

# Umoyo

**Nkhani 3**

hello@dignityonline.org.uk

+447340 573 937

## Kondani Muzinda Wanu!

Ndi coziswisa momwe anthu akhulupilira kuti alipo kuwasonkhaninsa iwo. Awona iye kunkhala Mulungu wa mphavu yonse amene ayembekezela ku weluza ndi ku zuzula anthu. Kuli awo anthu, afunikila kuyangana kwa Mateyu 23:37:

“Haa! Yerusalemu, Yerusalemu, iwe amene umapha aneneri ndi kugenda miyala amene atumidwa kwa iwe, kawirikawiri ndimafuna kusonkhanitsa ana ako, monga nkuku imasonkhanitsira ana ake, koma iwe sunafune.”

Yesu anayangana pa muzinda wa Yerusalemu nakumbukira ma chimo ya anthu. Angathe kuona zomwe anachita. Ngakhale kuti anapha omwe Mulungu anatuma, ndipo analinacho chifundo pa iwo ndi kulakalaka kuwatsonkhanitsa iwo pamodzi.

Kodi anazidwa ndi mkwiyo? Kodi anafuna kuti aononge muzinda? Iyayi! Eze anazidwa ndi chifundo ca anthu. Nthawi zambiri mmunzi ndi muzida wathu, tizonda ‘wochimwa’ - anthu omwe alinazo zikhulupirilo zisiyana kapena umoyonso osiyana kwa ife. Tiwaweruzwa ndiponso sitikhala nawo pamodzi. Nthawi zina tiwachotsa iwo m’makachitsi ndi m’midzi yathu. Uyu sindiye mukharidwe wa Yesu.

Iye anawaona kuti afunikila chisamarilo monga ana ankhuku. Ngakhale pomwe asanakonkhomoke, nkuku ikhala pamazira ndi kuwasunga wonthuma. Pomwe tu ana twakhuku tuli tung’ono zitudyetsa ndi kutusamalira mumaphiko zawo. Yesu alimonga izi ku anthu ake.

Ngakhale pomwe tachimwa, Mulungu afuna kuti ziwa ndi kutisamalira ife. Wamphavu wosatila wa Yesu, Paulo mutumwi, anena za chikondi cha Mulungu mu Aroma 5:8:

“Koma Mulungu anaonetsa chikondi chake kwa ife chifukwa pamene tinali ochimwabe, Khristu anatifera.”

Mulungu sanayembekezele ife kuti tikhale oyenera kwa iye. Anatifela ife ngakhale tinali wochimwa. Ngati Yesu sanataye ife kubwano, kodi ndi ufulu wabwanji omwe tilinawo kuchita chatero kwa ena? Yesu anali ndi chifundo ndipo naifeso tifunikila kukhala nacho kuli aliyetse ndiponso kwa onse otizungulira ife. Tifunikila ku konda ndipo tikhale nayo danga m’mudzi wanthu, osati kusutsana nalo!

### Ziyikeni mu Zocita!

Pangani chiwelengero cha aliyetse omwe inu kapenanso muzinda azonda kapenanso akanidwa ndipo muwaphelere. Pezani njira momwe mutha kuwadalisitsa – pezani nthawi kuti muwaziwe. Mwa izi, muzapeza dziko limodzi ndipo muzakwanitsa ku kula muchikondi ndiponso muchifundo kwa iwo.


### Pephelani kuti:

- 1) Azatha kuona chikondi cha Mulungu chikuwala mwa inu.
- 2) Muntha kuzazidwa ndi chifundo pa iwo.



“Pomwe tilikukhala tinali pafupi kusauka ndipo sitinali kuthandizana wina ndi mzake. Mulungu atithandizira kwambiri pamene tilikuleta bungwe la Dignity m’mudzi. Yanithandiza ine kuti ndi kusogorele kachitsi yanga mokoma.”

**- Myombo, Lubwe, Zambia**



Mphuziro iyi ndi yositsimusidwa ndi “Chikondi cha Mulungu” mphuziro yomwe ipezeka mu Kondani Mudzi wanu, ilipo pano:

**[dignityonline.org.uk/publications](http://dignityonline.org.uk/publications)**